

wosava kunena kwake Ambuye Mlungu watu, kuye ndaenda pa torah zake izo adaziika pa nkope zatu. *Dan.* ix. 9, 10.

Ambuye, unilange, nampo pa lamulo; posali pa kukwia, unganichepekeche. *Yer.* x. 24. *Zabur* vi. 1.

Mlape; pakuti Ufumu wa Kumwamba wawandikila. *W. Matt.* iii. 2.

Sindiime, sindiende ulendo kwa Atate wanga, ndipo siniti kwa iye, Atate, ndakulakwila Kumwamba, ndi pachogolo pako, wosayenedwancho kutanidwa mwana wako. *W. Luka* xv. 18, 19.

Usaloa pa kulamula pamoji ni kapolo wako, Ambuye; chifuko ali yenche wakulama wosatuluchidwa wa malinga pa nkope yako. *Zabur* cxliii. 2.

Tikati kuti tilije zambi, tijisokeza, ndipo va zene vosali pa ife: tikavumbula zambi zatu, wa mvano ali ndi wakuchita malinga kuti atilekele zambi zatu, ndipo atichuke ife kopanda malinga kuli konche. 1 *W. Yohana* i. 8, 9.

Abale wokondedwa viwi, Malembo yatichisa pena pena tisakana nampo tijiwiche ni kuvumbula zambi ni kuipa kwatu kwa makamu makamu; ndi kuti sitikadazishashaila, sitikadazivinikila pachogolo pa nkope ya Mlungu Mwene mpavu zonche Atate watu wa Kumwamba: nampo kuzivumbula ni mtima wakujichicha, wa panchi, wakulapa, ni wakuvecha; dala tipate kulekeledwa izi, kwa ubwino ni lisungu lake losali ni malile. Ndipo ingakale nyengo ili yonche tikadajiwicha chichichile zambi zatu pachogolo pa Mlungu; nampo maka maka tiyenedwa kuchita chimwechi, yapo tisonkana ni kukomana pa bwalo kuyamika kwa ivo vavikulu vakutikomela ivo tavilاندila pa manja yake, kubukicha malumbo yake maka maka yoyenedwa, kuvera Mau lake loyera

## MAIKIDWE YA SALA ZA UJULO, SIKU NI SIKU PA NYENGO ZONCHE ZA CHAKA.

¶ *Pa kuyamba Sala za Ujulo Wotumikila Mlungu ngati anyamata wake ajiwerenga ni mau yakulu Sentences izi zina zina ingakale imoji ingakale zakupunda za Malembo izi zichatazo. Ndipo pa nyengo ija ajinena yaja yalembedwa pambuyo pa Sentences zija zakuti zakuti.*

Pa kubwela wakuipa pa kuipa kwake kuja amachita, nakachita malamulo ni kuchita malinga, mmweyo salamiche umoyo wake. *Ezek.* xviii. 27.

Ndijiwicha cholakwa changa, ndi zambi yanga ilipo pachogolo panga chichogolele. *Zabur* li. 3.

Bisa nkope yako kwa zambi zanga, ni ukatime zimpulupuli zanga zonche. *Zabur* li. 9.

Nchembe zodula za Mlungu roho yosweka: mtima wosweka ni wopondeka, Mlungu, suupepula. *Zabur* li. 17.

Ng'ambani mtima wanu, yosali malaya yanu, mka-mbwelele Ambuye Mlungu wanu: chifuko mmweyo mwene neema ni mwene lisungu, wakuzengeleka kukwia, ni wochuluka ubale, ni wakulapa kwa choipa. *Yoel* ii. 13.

Kwa Ambuye Mlungu watu kuli malisungu ni vakuteteza, ingakale tamasula mwendo kwake: ndipo

viwi, ni kupempa ivo sivifunidwe ni sivingasiidwe, umo kwa tupi mmwemo kwa umoyo ncho. Mmwemo ndikupempani ni kukupembezeni inu, monche mulipo pano, kuchatana ndi ine ni mtima wochuki-dwa, ni mau yakujichicha, ku mpando wa neema ya Kumwamba, kunena pambuyo pa ine ;

¶ *Kuvumbula zambi ngati kwa kamu kukadanenedwa ndi Gulu la Church tenyu pambuyo pa Wotumikila Mlungu, chigwadile wonche.*

Atate mwene mpavu zonche ndi mwene lisungu lakupunda; taponya, ni tasokelela pa njila zanu ngati mbelele zotaika. Tachata nditu maganizo ndi vokumbila va mitima yatu. Takuchimwichani pa matauko yanu yoyera. Tavisia vosachitidwa ivo tiyeneledwa kuvichita; Tachita ivo sitinayeneledwa kuvichita; Ndi pa ife kusangalala paliye. Nampo Imwe, Ambuye, mtilengele lisungu, ife wakuchwalicha wosauka. Mwalekele, Mlungu, yawo wavumbula volakwa vao. Mwabweze yawo walapawo; Kwa malangano yanu mdawanenela wana wa adam pa Kristo Yesu Ambuyatu. Ndipo mtilenjele, kwa chifuko chake, Atate wa lisungu lakupunda; Chiyambile lelo, kulama ife pa kukutumikilani Imwe, pa kuchita malinga, ni pa kujikoza, Likuzidwe Jina lanu la pa loka. Amen.

¶ *Kumasula, kapena Kulekela zambi, kunenedwa ngati pa bwalo ndi Kasis yeka, chiimile; kamu chikalile pa kugwadila.*

Mlungu mwene mpavu zonche, Atate wa Ambuyatu Yesu Kristo, wosafuna mwene zambi afe, nampo ang'anamuke kusia voipa vake, ndipo alame; ndi awaninka Wotumikila wake bwalo, ni tauko, wafoto-kozele ndi wanenele ngati pa bwalo kamu lake, akalapa, Kumasula ndi Kulekela zambi zao: Iye osasungila milandu ndi awamasula wonche yawo alapa kwa zene, ndi wavomela wosazimbaicha

Evangel yake yoyela. Chifuko ichi timpembeze atii pache kulapa kwa zene, ndi Roho wake woyela, kutvintu ivo tichita chapano, vimkondweche; ndi kulama kwatu uku kukalapo chiyambile lelo kukale kopanda ukazuzi, ndi koyela; kuti tifike pa kutela kwa kusangalala kwake kwa masiku yonche; mkati mwa Yesu Kristu Ambuyatu. Amen.

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu ajigwada, ndi ajinena pempelo la Ambuye pa mau yakuweka; kamu ncho chigwadile, ndi kulinenancho pamoji ndi iye.*

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku. Ndi utilekele mangawa yatu, ngati ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa; Nampo utipulumuche pa voipa: Chifuko ufumu, Ndi mpavu, Ndi kukuzika vili vako, vyaka vosata. Amen.

¶ *Ndipo chimwechi ajinena,*

Ambuye, mmasule milomo yatu.

*Yanko.* Ndi kamwa latu silikulumbeni.

*Kasis.* Mlungu, msazengeleka kutipulumucha.

*Yanko.* Ambuye, wirimani kutitangatila.

¶ *Yapa wonche chiimile, Kasis ajinena,*

Akuzike Atate, ndi Mwana: ndi Mzimu Woyela;

*Yanko.* Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano: ndi kwa vyaka vosata. Amin.

*Kasis.* Alumbeni Ambuye.

*Yanko.* Jina la Ambuye lilumbidwe.

¶ *Ndipo zijinenedwa kapena zijimbidwa Zabur pa mpingo wao umo zalangizidwila. Ndipo Somo la Malangano ya Kale, umo lalangizidwila. Ndi pambuyo pake, Magnificat (kapena Nyimbo ya Woyerekedwa Virgin Mary) pa Chinyanja, umo yachatila.*

MAGNIFICAT. *W. Luka i.*

Umoyo wangu umkuzicha Ambuye : mzimu wanga wasekelela pa Mlungu Mpulumuchi wanga.

Chifuko waupenya : ung'ono wa kapolo wake.

Pakuti penya, chiyambile lelo : vibadwa vonche sivinitane mwene mwawi.

Chifuko mwene mpavu adanichitila yakulu : ndi Jina lake lili pa loka.

Ndi lisungu lake lili mpaka vibadwa ni vibadwa : kwa yawo wakumuopa.

Adachita mpavu kwa janja lake : anawamwaza wojitwinya pa maganizo ya mitima yao.

Anawachocha wene mpavu pa mipando yao : anawanyamula yawo wali panchi.

Anawakuticha ni vabwino wakuona njala : anawapacha mwanja wakuina manja ya chomwe.

Adamtangata Israel mnyamata wake, kukumbukilila Abraham ndi mbeu yake ya vyaka lisungu : umu adakambila ni achatate watu.

Akuzike Atate, ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Pena Zabur iyi ; ikawe pa Siku ya Kumi ni kenda ya Mwezi, yapo iwerengedwa pa Mpingo wokonjedwa wa Zabur.*

CANTATE DOMINO. *Zabur xcvi.*

Mwimbileni Ambuye nyimbo ya chapano : kuti anachita vopambana.

Janja lake la chimuna, janja la kuyela kwake : lidamchitila upulumuchi.

Ambuye waujiwicha upulumuchi wake : umu achitila malinga anavunukula pa maso ya mafuko.

Anakumbukila ubale wake ni mvano wake kwa nyumba ya Israel : vinchonga vonche va jiko vauona upulumuchi wa Mlungu watu.

Mkuzileni Ambuye, maiko yonche : gamukani, lulutani, ndi imbani zabur.

Mwimbileni Ambuye zabur ni chilumbo : ni chilumbo ni pokoso la zabur.

Ni mbetete ni pokoso la lipenga : kuzani pa nkope ya Ambuye Mfumu.

Nyanja ilindime, ni vonche vijalamo : mondo, ndi yawo wakalamo.

Michinje iombe mmanja, ndi mapili yalulute pamoji pa nkope ya Ambuye : chifuko akuja kulamula jiko.

Salamule mondo pa kutchita malinga : ni makamu pa vakuongoka.

Akuzike Atate, ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Ndipo Somo la Malangano ya Chapano umu yalanguzidwila. Ndi pambuyo pake, Nunc Dimittis (pena Nyimbo ya Symeon) pa Chinyanja, umu muchatilamo.*

NUNC DIMITTIS. *W. Luka ii. 29.*

Chapano uniwelukiche kapolo wako, Ambuye : umu udanenela, pa mtendele.

Chifuko maso yanga : yauona upulumuchi wako Uja unaikilatu : pa maso pa makamu yonche ;

Dangalila kuvunukulila Mafuko : ndi kukuzika kwa kamu lako Israel.

Akuzike Atate, ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Pena Zabur ii : ikawe pa Siku ya Kumi ni kawili ya Mwezi.*

DEUS MISERATUR. *Zabur lxxvii.*

Mlungu atichitile neema, akatipache mwawi : amulikiche nkope yake kwa ife ;

Njira yako ijiwike muno mjiko : upulumuchi wako pa mafuko yonche.

Makamu yabukiche mbiri yako, Mlungu : wabuki. che mbiri yako makamu yonche.

Waseke ndi walulute vilawa : chifuko suwalamule makamu chiongokele, ni vilawa va jiko suwachogoze.

Makamu yonche wabukiche mbiri yako, Mlungu : makamu yonche wabukiche mbiri yako.

Jiko lapeleka vipacho vake : satipache mwawi wa Mlungu, Mlungu watu.

Satipache mwawi Mlungu : ndi vinchonga vonche va jiko sivimwope.

Akuzike Atate, ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

¶ *Ndipo ujinenedwa kapena ujiimbidwa Mvano wa Apostolo ni Wotumikila Mlungu ni kamu, chiimile.*

Ndimvomela Mlungu Atate Mwene mpavu zonche, Wopanga Kumwamba ndi jiko :

Ndi Yesu Kristo Mwana wake yeka yeka Ambuye watu, Uyo adatengedwa mimba ndi Mzimu Woyela, Wobadwa ndi Maryamu Virgin, Wosauchidwa pa nyengo za Pontio Pilato, Wotalamichidwa pa msalaba, wakufa, woikidwa pa manda, Adachika pa malo pa mizimu ; Siku la katatu adazyuka pa wakufa, Adakwela Kumwamba, Ndi akala panchi pa janja la kwene la Mlungu Atate Mwene mpavu zonche : Kuchoka kumweko saaje kulamula wakulama ndi wakufa.

Ndimvomela Mzimu Woyela ; Church Loyela ndi Katoliko ; Kusanganizana kwa Woyela ; Kulekeledwa zambi ; Kuzyuka kwa tupi, Ndi kulama kwa vyaka. Amen.

¶ *Ni pambuyo pake, mapempelo aya yachatayo, wonche kugwada chipembezele ; Wotumikila Mlungu kunena pachogolo ngati pa bwalo ni maru yakulu,*

Ambuye akale ndi inu.

*Yanko.* Akale ndi mzimu wako.

*Wotumikila.* Tipempe.

Ambuye, mtilengele lisungu.

*Kristo, mtilengele lisungu.*

Ambuye, mtilengele lisungu.

¶ *Ndipo Wotumikila Mlungu, aKleriko, ni kamu, wajinena Pempelo la Ambuye ni maru yakulu.*

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku. Ndi utilekele mangawa yatu, ngati ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa ; Nampo utipulumuche pa voipa. Amen.

¶ *Ndipo Kasis chiimile ajinena.*

Mtilangize, Ambuye, lisungu lanu.

*Yanko.* Mtipache upulumuchi wanu.

*Kasis.* Ambuye, mmsunge Mfumu.

*Yanko.* Mtiveche kwa lisungu, yapo tikakutani-lani.

*Kasis.* Mwaveke Wotumikila wanu ndi kuchita malinga.

*Yanko.* Mwasangalaliche wosankidwa wanu.

*Kasis.* Mwasunge kamu lanu, Ambuye.

*Yanko.* Mwapache mwawi wantu wa chokolo chanu.

*Kasis.* Mpeleke mtendele, Ambuye, pa masiku, yatu.

*Yanko.* Chifuko paliye mwina wakutiimilila ni nkondo, nampo Iwo Mlungu watu.

*Kasis.* Mlungu, mchite mitima yatu yochukidwa.

*Yanko.* Ndi Mzimu wanu Woyela msatichochela.

¶ *Ndipo yajichata mapempelo ya chidule yatatu; lakuyamba la Siku; la kawili kwa Mtendele; la katatu kuti titangatidwe kuviombela voluswa vonche, umo muchatilamo; mapempelo ya chidule yaja yawili yakutera yajinenedwa siku ndi siku pa Sala za Ujulo yosang'anamulidwa.*

*Pempelo la chidule la kawili pa Sala za Ujulo.*

Mlungu, kuchokela kwanu vofunila vonche voyela, malango yonche yabwino, ndi nchito zonche za malinga; Mwapache akapolo wanu mtendele uja jiko lino losakoza kuupacha; ndipo mitima yatu ikapelekedwa kwa kuvela matauko yanu, ndi sonincho mkatiombelala manta ya wa mawongo watu, tikaliletu pa kupuma ndi popanda milandu; kwa kuyenela kwake Yesu Kristo Mpulumuchi watu. *Amen.*

*Pempelo la chidule la katatu, kuti titangatidwe kuombela voluswa vonche.*

Tikupembezani, Ambuye, mmulike mmdima mwatu; ndipo mtisunge kwa lisungu lanu lalikulu pa voluswa ndi vipandu vonche va usiku uno; kwa kukonda kwake Mwana wanu yeka yeka, Mpulumuchi watu, Yesu Kristo. *Amen.*

¶ *Pa Quires ni pa Mbuto yapa waimba, apa ijichata Anthem.*

*Pempelo kwa ukulu wake Mfumu.*

Ambuye Atate watu wa Kumwamba, wa pamwamba ndi mwene mpavu, Mfumu wa mafumu, Ambuye wa achambuye, mwoka Wakulinganicha anduna, pa mpando wanu mzuzumila wonche wakukala pa jiko; Ndi mitima yatu nditu tikupembezani kupenya ni neema yanu Sovereign Ambuye watu mwene neema maka maka, Mfumu \*.....ndipo mmzaze ni neema ya Roho wanu Woyela, mpaka siku zonche

\* 1. Edward. 2. Manuel. 3. William.

atembenukile umo mfunila, ndi ayendende pa njila yanu: Mmveke ni vintu va chomwe vohuluka vakuchoka Kumwamba; alame mkulamaje pa kusangalala ni kufanikila; mmtilile mpavu alake ni kupunda wonche wamaongo wake; ni pakutera pambuyo pa kulala pano, apatile chimwemwe chikalile mmwemoje chikondele; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Pempelo kwa wa mnyumba ya mfumu.*

Mlungu mwene mpavu zonche, chitime cha vabwina vonche, pa kujichicha tikupembezani kumpacha mwawi Mfumu kazi watu mwene neema \*.....ndi wonche wa mnyumba ya Mfumu: mwaveke ni Roho wanu woyela; mwaninke chuma cha neema yanu ya Kumwamba; mwafwanikiche ndi kukondwa konche; ndi mwatengele ku ufumu wanu wa chikalile mmwemoje; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Pempelo kwa a kleros ndi kamu.*

Mlungu mwene mpavu zonche wa vyaka vosata, mchita videlu vavikulu moka; Mtume panchi kwatulila AAskof watu, ni Wosungila, ndi Magulu ya Church yonche yaikidwa mmanja mwao, Mzimu wakusangalalicha wa neema yanu; ndipo dala wakukondwecheni kwa va zene, mwapungulile wosapuma chime cha mwawi wanu. Mtipache ichi, Ambuye, kwa kumyinikiza Woimilila watu ndi Wotiteteza, Yesu Kristo. *Amen.*

*Pempelo la Woyela Krusostomo.*

Mlungu mwene mpavu zonche, mwatipacha neema nyengo ii kuchita kwa mtima umoji mapembezo yatu yakusanganizana pachogolo panu; ndi mwalanga kuti wawili kapena watatu wakasonkana kuchamila Jina lanu simwapache ivo wafuna: Mmalize chapano, Am-

\* 1. Alexandra 2. —. 3. Victoria.

buye, ivo wafuna ndi ivo wapempa akapolo wanu, umo simuwakomele viwi; kutipachaje pa vyaka ivo vilipo tijiwe va zene vanu, ndi pa vyaka vija sivije kulama kwa vyaka vosata. *Amen.*

2 Kor. xiii.

Neema ya Ambuyatu Yesu Kristo, ndi kukonda kwake Mlungu, ni kusanganizana kwa Mzimu Woyela, kukale ndi ife tonche kwa vyaka vosata. *Amen.*

*Apa yatela marikidwe ya Sala za Ujulo pa nyengo zonche pa Chaka.*

## PA SALA ZA UMAWA.

¶ *Pa Siku izi zazikulu; Christmas-Day, Epiphany, W. Mattiya, Siku ya Paska, Siku ya Kukwela, Siku ya Pentekote, W. Yohana Baptist, W. Yakobo, W. Bartolomayo, W. Mattayo, W. Simon ni W. Yehuda, W. Andrea, ni pa Siku la Ambuye la Utatu, yaji-imbidwa kapena yajinenedwa pa Sala za Umawa, pa malo ya Mvano wa AApostolo, mau aya yakuturucha Mvano watu wa ChiKristo, ayo wazoweleda kutana Mvano wa W. Athanasio, Wotumikila Mlungu ndi kamu, chiimile.*

## QUICUNQUE VULT.

Ali yenche afuna kukala wopulumuchidwa : pa chogolo pa vonche sangasie kugwila bwino Mvano Katoliko.

Mvano uu muntu akapanda kuusunga wotelanya ndi wosatilidwa cha chaje : popanda kukaikila sataike chikalileje.

Ni Mvano Katoliko ndio uu : kuti timlambile Mlungu mmoji pa Utatu, ndi Utatu pa Umoji;

Wosatimbilikanya Achinawene : wosachigawa Chitulo.

Pakuti Mwene wake wa Atate ali wina, ni wa Mwana ali wina : ni wa Mzimu Woyela ali wina.

Nampo Umlungu wa Atate, wa Mwana, ni wa Mzimu Woyera, uli umoji : Kukuzika kwakulingana, Ukulu chikalileje pamoji.

Wa mtundu Atate ali, wa mtundu umweo ni Mwana : ndi wa mtundu umweo Mzimu Woyela.

Atate wosapangidwa, Mwana wosapangidwa : ni Mzimu Woyela wosapangidwa.

Atate wopanda malile, Mwana wopanda malile : ni Mzimu Woyela wopanda malile.

Atate wa chikalileje, Mwana wa chikalileje : ni Mzimu Woyela wa chikalileje.

Nampo palije watatu wa chikalileje : mmoji nampo wa chikalileje.

Chimwechija palije watatu wopanda malile, ingakakale watatu wosapangidwa : mmoji nampo wosapangidwa, ni mmoji wopanda malile.

Chimwechija Atate mpavu yene, Mwana mpavu yene : ni Mzimu Woyela mpavu yene.

Nampo palije watatu mpavu yene : mmoji nampo mpavu yene.

Chimwechija Atate Mlungu, Mwana Mlungu : ni Mzimu Woyela Mlungu.

Nampo wopanda Achimlungu watatu : Mlungu mmoji nampo.

Chimwechija Atate Ambuye, Mwana Ambuye : ni Mzimu Woyela Ambuye.

Nampo palije Achambuye watatu : mmoji nampo Ambuye.

Chifuko umo tichunguzidwila kwa ivo va zene va Chi Kristo : kumvomelecha Mwene wake ali yenche pa yeka Mlungu ni Ambuye.

Mmwemo tikanizidwa ni Religion Katoliko : kumvomelecha Mwene wake ali yenche pa yeka Mlungu ni Ambuye.

Atate wosachitidwa kuchoka pa ali yenche : wosapangidwa, wosabalidwa.

Mwana ali wa kuchoka pa Atate yeka : wosachitidwa, wosapangidwa, nampo chibalidwile.

Mzimu Woyela wakuchoka pa Atate ni pa Mwana : wosachitidwa, wosapangidwa, wosabalidwa, nampo chitulukileje.

Chimwechi Atate mmoji, wosali Achatate watatu ;

Mwana mmoji, wosali Wana watatu : Mzimu Woyela mmoji, wosali Wazimu Woyela watatu.

Ni pa Utatu uu palije cha pachogolo, ingakale cha pambuyo : palije chakupunda, ingakale chakuchepa ;

Nampo Achinawene watatu wa mpumpu wali chikalile mmwemoje : ni wakulingana pamoji.

Chimwechi ponche ponche, umo yanenedwela pamwamba : Umoji pa Utatu, ni Utatu pa Umoji ukadalambilidwa.

Mmwemo iye afunaye kukala wopulumuchidwa : akadaganizila Utatu chimwechi.

Sonincho, kwa kupulumukilatu mmwemoje chosasiika : kuvomela chivomelele umo Ambuye watu Yesu Kristo adachitidwila Nyama.

Pakuti Mvano woongoka ni kuti, tivomele ni tivumbule : kuti Ambuye watu Yesu Kristo, Mwana wa Mlungu, ali Mlungu ni Muntu ;

Mlungu ali, kutuluka pa Chitulo cha Atate, wobadwa pachogolo pa zinyengo : ni Muntu ali, kutuluka pa Chitulo cha Amake, wobadwa pa zinyengo ;

Mlungu chimalizikile, ndi Muntu chimalizikile : chikalile ni chitulo kutuluka pa umoyo wene njelu ni nyama ya wana wa adam ;

Wolingana ni Atate, panama Umlungu wake : wosafelana ni Atate, panama Umuntu wake.

Uyo nangakale Mlungu ni Muntuncho : nampo wosali wawili, Kristo mmoji ali ;

Nampo mmoji ; wosali pakung'anamuka Umlungu chiloele mnyama : nampo pa kuutola Umuntu kuloa mUmlungu ;

Mmojidi ; wosali pa kutimbilikanya chitulo : nampo pa Mwene wake kukala mmoji.

Chifuko ngati umoyo wene njelu ni nyama zili muntu mmoji : chimwechi Mlungu ni Muntu Kristo mmoji ali ;

Uyo anava masaucho dala kutipulumucha : adachika

pa malo ya mizimu, adazyuka siku ya chitatu pa yawo wakufa.

Adakwela Kumwamba, naye akala pa janja la kwene la Atate, Mlungu Mpavu yene : kuchokela kumweko saaje kuwalamula wakulama ni wakufa.

Pa kuja kwake wantu wonche siwadazyuke ni matupi yao : ndipo sataulile ya nchito izo wanazichita achinawene.

Ni iwo wanachita vabwino saloe pa kulama mmwemoje : nampo iwo wanachita voipa pa moto wa mmwemoje.

Uu ndio Mvano Katoliko : uwo ali yenche akapanda kuuvomela chivomelele, wosakoza kukala wopulumuchidwa.

Akuzike Atate ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi chapano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

## LITANIA.

¶ Apo lichata Litania, kapena Mapembezo ngati kwa Kamu, kuimbidwa kapena kunenedwa pambuyo pa Sala za Umawa pa Siku za Ambuye, Wednesdays ndi Fridays, ndi pa nyengo zina yapo silitaukidwe ni Mwene kuika.

Mlungu Atate, wa kumwamba : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.

*Mlungu Atate wa kumwamba : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.*

Mlungu Mwana, Wakuliombola jiko : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.

*Mlungu Mwana, Wakuliombola jiko : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.*

Mlungu Mzimu Woyela, wa chitulukileje mwa Atate ni mMwana : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.

*Mlungu Mzimu Woyela, wa chitulukileje mwa Atate ni mMwana : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.*

Utatu Woyela, Wene mwawi, Wokuzika, Achinawene watatu ndi Mlungu mmoji : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.

*Utatu Woyela, Wene mwawi, Wokuzika, Achinawene watatu ndi Mlungu mmoji : mtilengele lisungu ife tisauka wene zambi.*

Msakumbukila Ambuye, vochwalicha vatu, ingakale vochwalicha vya achatate watu wa chikale ; ingakale msajilipilila pa zambi zatu : mtilekele ife, Ambuye wabwino, mwalekele kamu lanu, ilo mwalio mbola ni mwazi wanu wa mtengo wokulu, ndipo msakwia ndi ife vyaka vonche.

*Mtilekele ife, Ambuye wabwino.*

Pa choipa chili chonche ni malindi ; pa zambi, pa



kuchenjera ni kuulukila kwake diabolo ; pa kupyecha mtima kwanu, ni pa kulamula chilamulileje,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Pa kupulika maso konche pa mtima ; pa kujikwisa, ni kujiyerekele chaje, ndi kujizimbaicha ; pa kupweteke mtima, kulunduka, ni kufinga, ndi pa kuchepa konche kwa kukondana,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Pa vyasa, ni zambi zonche zina za kutipa ; pa vakutinyengeza vonche va mjiko, ni va nyama, ni va diabolo,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Pa kung'anipa mpambe ni chimpunga ; pa kufa kwa mtimbo wanu, pa chipindu-pindu, ndi pa chilala ; pa kuungana nkondo ndi kusinikalila, ndi pa kufa kwa chizilimukila,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Pa kuchucha mfumu chaje, kupangana malindi, ndi kumasula mwendo ; pa kuyeruza unama, kujisankulila, ni kujipatula ; pa kuumicha mtima, ndi kupepula Mau lanu ni Tauko,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Kwa mau la kuseli yapo mwachitidwa Nyama moyera ; kwa Kubadigwa kwanu koyera ndi Kuumbalidwa ; kwa Ubatizo wanu, Kujimana chakudya, ndi Kuyesedwa,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Kwa Kuchilichimba kwanu, ndi Chitukuta chija cha mwazi ; kwa Msalaba wanu ndi Kuva masaucho ; kwa Kufa kwanu kwene mtengo ndi Kuikidwa pa manda ; kwa Kuzyuka kwanu kwene kukuzika ndi Kukwela kumwamba ; ndi kwa kuja kwake Mzimu Woyera,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Pa chaka chonche cha kusauka kwatu ; pa chaka chonche cha kufanikila kwatu ; pa hour ya kufa, ndi pa siku ya kulamula,

*Ambuye wabwino, mtipulumuche.*

Ife wene zambi tikupembezeni kutivera, Ambuye Mlungu ; ndi mlole kulilinganicha ni kuliongola Church lanu loyera lakuyenela ponche pa njila ya kuongoka ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kwasunga ni kwalimbicha pa kukulambilani kwene kwene, pa kuchita malinga ni pa kuyera pa kulama, kapolo watu \* . . . , Mfumu watu mwene neema nditu ni Wakutiongola ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kulinganicha mtima wake pa mvano wanu, manta yanu, ni chikondano chanu, ndipo chiyambile chapano akukulupilileni, ndipo afune-fune chifunile kuyinikiza kwanu ni kukuzika ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kumombelela ni kumsunga, kumpacha kwalaka wonche wa mawongo wake :

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kwapacha mwawi ni kwalindilila Mfumu kazi mwene neema † . . . ni wonche wa mnyumba ya mfumu ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kuwamunikila wonche AAskof, AKasis, ni AShemas, ni kujiwa ni kuzindikila kwene kwa Mau lanu ; ndipo pa kuyeneza ndi pa kulama kwao neho walibukiche pa bwalo, ndipo walilangize mmwemo ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kwaveka Ambiri wonche wa Bwalo la Mfumu, ni Afuru wa makamu wojiwika, ni neema, njeru, ni kuzindikila ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

Mlole kwapacha mwawi ni kwasunga yawo Wopachidwa bwalo, kwapacha neema wachitiletu ya malinga, ni kuimilila va zene ;

*Ambuye wabwino, tikupembezeni kutivela.*

\* 1. Edward. 2. Manuel. 3. William.

† 1. Alexandra. 2. ——. 3. Victoria.

Mlole kuwapacha mwawi ndi kulisunga kamu lanu lonche ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kuwapacha mafuko yonche kuunjikana pamoji, mtendere, ndi kuilana pa mitima ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kutipacha mtima kukukondani ni kukuopani, ndi kuchita njeza kulama kwa mlingo wa matauko yanu ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kuwaonjezela kamu lanu lonche neema kulivecha modeka Mau lanu, alilandile ni kukonda kwene, ndi kupacha vipacho va Roho ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kulovya m'njira ya va zene wonche yawo wasokelela, ndi wanyengedwa ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kulimbicha wonche yawo wali mkuima ; ndi kwatontoza ndi kwatangata wolenda m'mitima ; ndi kwaucha yawo wakugwa ; ndi pa kutera kumfinga Shetan panchi pa mapazi yatu ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kwapakola, kwatangatila, ndi kwatontoza, wonche yawo ali pa kuluswa, pa kusowa vintu, ndi pa kulaga ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kusunga wonche ali mkuyenda ulendo pa mtunda pena pa nyanja, wakazi wonche yawo ali mkupuma wana, wonche wakudwala, ndi wana wakanda ; ndi kuwalengela lisungu lanu wonche yawo wamangidwa ni wa mikoli ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kwaombelega, ndi kwalela, wana wonche wa masiye, ndi anamfedwa, ndi wonche woingwa ni wosauchidwa ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kuwalengela wantu wonche lisungu ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kuwalekela wa mawongo watu, yawo wakutitamangicha, ndi yawo wakutigumulila, ndi kung'anamula mitima yao ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kutininka ni kulindilila vipacho va jiko umo vibadwila tivitumile, kuti pa nyengo yake yakukwima tijikondwele navo ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mlole kutipacha kulapa kwene ; kutilekera zambi zatu zonche, kupungwaila, ndi kopanda kujiwa ; ndipo mtiveke ni neema ya Roho wanu Woyera, tikonje makalidwe yatu kwa mlingo wa Mau lanu loyera ;

*Ambuye wabwino, tikupembezani kutivela.*

Mwana wa Mlungu : tikupembezani kutivera.

*Mwana wa Mlungu : tikupembezani kutivela.*

Kambelele ka Mlungu : wakuzichocha zambi za jiko ;

*Mtipache mtendele wanu.*

Kambelele ka Mlungu : wakuzichocha zambi za jiko ;

*Mtilengele lisungu.*

Kristo, mtivele.

*Kristo, mtivele.*

Ambuye, mtilengele lisungu.

*Ambuye, mtilengele lisungu.*

Kristo, mtilengele lisungu.

*Kristo, mtilengele lisungu.*

Ambuye, mtilengele lisungu.

*Ambuye, mtilengele lisungu.*

¶ Ndipo kasis, ndi kamu pamoji naye, wajinena pempelo la Ambuye.

Atate watu, wa Kumwamba, Jina lako liyelechedwe. Ufumu wako uje. Vija ufuna vichitidwe, mjiko ngati Kumwamba. Utipache lelo chakudya chatu cha siku. Ndi utilekele mangawa yatu, ngati

ife tiwalekela wa mangawa watu. Ndi usatitengela poyesedwa ; Nampo utipulumuche pa voipa. Amen.

*Kasis.* Ambuye, msatichitila umo tinachitila zambi.

*Yanko.* Msatilipilila umo tinachitila zimpulu-pulu.

### Tipempe.

Mlungu, Atate mwene lisungu, wosapepula kubu-  
ula kwa yawo wakutimbinyuka mtima, ingakale  
kufuna kwa yawo wadandaula ; Kwa lisungu mtiimi-  
lile pa mapempelo yatu yayo tiyachita pa maso yanu  
pa masauko ni maputo yatu yonche, pali ponche yati-  
lemelela ; ndipo mtivele kwa neema kuti voipa vija,  
ivo kuchenjela ni kunyengeza kwa diabololo kapena  
kwa wantu kutichitila, vilazidwe chaje ; ndi kwa  
malango ya ubwino wanu vimwazike nditu ; kuti ife  
akapolo wanu, tikapanda kupwetekechedwa ni mata-  
mangichidwe yali yonche, tisapuma kukuyamikani  
pa Church lanu loyera ; mkati mwa Yesu Kristo  
Ambuyatu.

*Ambuye, ukani, mtitangatile, ni mtivuule chifuko cha  
Jina lanu.*

Mlungu, tavera ni makutu yatu, ndi achatate watu  
wadatifotokozela, vija va ufulu mnachita masiku yao,  
ni masiku ya kale pachogolo pa achi-iwo.

*Ambuye, ukani, mtitangatile, ni mtivuule myini-  
kizidwe.*

Akuzike Atate, ndi Mwana : ndi Mzimu Woyela ;

*Yanko.* Umo kumakalila poyamba, chimwechi ndi  
chapano : ndi kwa vyaka vosata. Amen.

Pa wa mawongo watu mtiombelele, Kristo.

*Mtipenye pa kulaga ni mtima wa ufulu.*

Kulira kwa mtima watu mpenye wene lisungu.

*Wene ubale msaziumila zambi za kamu lanu.*

Chilolele wene ubale mvere kupempera kwatu.

*Mwana wa David, mtichitile lisungu.*

Ndi chapano ni chikalile mmwemoje muone mwa-  
yeneledwa kutivera, Kristo.

*Mtivele kwa neema, Kristo ; mtivele kwa neema,  
Ambuye Kristo.*

*Kasis.* Ambuye, lisungu lanu lilangizidwe pa ife ;

*Yanko.* Umo ife tikukulupililani.

### Tipempe.

Tikupembezeni mojjichicha, Atate, kupenya chite-  
tezele kuti ife wosali ndi mpavu ; ndipo Jina lanu  
likuzidwe mng'anamule pa ife voipa vija vonche ivo  
tayeneledwa kuvipata kwa malinga nditu ; ndi mti-  
pache, kuti pa masauko yatu yonche tikulupilile  
chikulupilile wosaopa pa lisungu lanu, ndipo chiya-  
mbile chapano tikupoteleni pa kukala wa pa woka ni  
wopanda ukazuzi, myinikizidwe ni kukuzidwa ; mkati  
mwa Woteteza watu ndi Woimila wa pa yeka, Yesu  
Kristo Ambuyatu. Amen.

### *Pempelo la Woyela Krusostomo.*

Mlungu mwene mpavu zonche, mwapipacha neema  
nyengo ii kuchita kwa mtima umoji mapembezo yatu  
yakusanganizana pachogolo panu ; ndi mwalanga  
kutii wawili kapena watatu wakasonkana kuchamila  
Jina lanu simwapache ivo wafuna : Mmalize chapano,  
Ambuye, ivo wafuna ndi ivo wapempa akapolo wanu,  
umo simuwakomele viwi ; kutipacha pa vyaka ivo  
vilipo tijiwe va zene vanu, ndi pa vyaka vija sivije  
kulama kwa vyaka vosata. Amen.

### 2 Kor. xiii.

Neema ya Ambuyatu Yesu Kristo, ndi kukonda  
kwake Mlungu, ni kusanganizana kwa Mzimu  
Woyela, kukale ndi ife tonche kwa vyaka vosata.  
Amen.

APA LITELA LITANIA.

kukonja makalidwe yatu pano, ni sonincho kwa lisungu lanu kukulumbani ni kukukuzichani; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Pa nyengo ya Namba chakudya ni chilala.*

Mlungu, Atate watu wa Kumwamba, imwe wene mpeleka vula ivumbe, jiko lipache vopacha, nyama zibalane, ni nchomba zionjezeke; Penyani, tikupembezeni, masauko ya kamu lanu; ndi mtipache kuti kusowa vintu ni namba chakudya, izo tayeneledwa kusauchidwa nazo chifuko cha mpulimpuli zatu, zisanduchidwe kwa ubwino wanu chilengelele lisungu kukala malonda yosauma ndi chindimba; kwa kunda kwake Yesu Kristo Ambuyatu, kwa Uyo pamoji namwe ni Mzimu Woyela kukale kuyinikiza ni kukuzicha, chapano ndi chikalile mmwemoje. *Amen.*

*Kapena ili.*

Mlungu, Atate mwene lisungu, mwawenu pa siku za Elisha wolosa, mdatembenuza chizizimukile kuso wa vintu viwi ni namba chakudya pa Samaria kukala chindimba ni malonda yosauma; Mtilengele lisungu, kuti ife, pakulangidwa chapano kwa zambi zatu ni masauko ngati yaja, tilenjele chimwechija tawefe titangatidwe pa nyengo yake: Muvionjezele vipacho va jiko kwa kupeleka mwawi wanu wa Kumwamba: ndipo mtinike kuti ife, tikalandila ivo va kukoma pakosi kwanu kosamana, tichite navo kuti mkuzike mawene, wa mpawi watangatidwe, ni mitima yatu tawefe itontozedwe; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Pa nyengo ya Nkondo ni Mapokoso.*

Mlungu Mwene mpavu zonche, Mfumu wa mafumu wonche, ndi Wakuviongola vintu vonche, mpavu zanu namba chintu chili chonche chopangidwa chikoza kuchucha, kuliko kwa Imwe kulanga wene zambi kwa malinga, ni kuwalengela lisungu yawa wakulapa kwa

## MAPEMPELO NI MAU YA YAKUYAMIKA

PA IVO VIKUGWAVO VINA VINA.

¶ *Yakadanenedwa pachogolo pa mapempelo yawili yakutela ya Litania, kapena ya Sala za Umawa ndi za Ujulo.*

### MAPEMPELO.

*Kupata vult.*

Mlungu, Atate wa Kumwamba, mwalanga kwa Mwana wanu Yesu Kristo, kuti, siniwaninke wonche yawo wafunafuna ufumu wanga, ni kuchita malinga kwa mlingo wake, vintu vonche ivo sivifunidwe kulela tupi lao; Mtipelekele, tikupembezeni, pa kusowa chimwechi, vula ya msinku ni ya nyolinyoli, kuti tilandire vipacho va jiko kutitontoza ife, ni kwa kukulemekezani: mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kupata ng'amba yabwino.*

Ambuye Mlungu Mwene mpavu zonche, kale chifuko cha zambi za wana wa adam mdagwibilicha jiko lonche, akawe wantu asano ni atatu, ndipo pambuyo pake kwa lisungu lanu lalikulu mdalanga, kuti wosaliona ngancho; Ife tikupembezeni chichikile, kuti, ingakale ife tayeneledwa chiyeneledwele kwa zimpu-lumpulu zatu kutimbidwa ni mtimbo wa vula ni maji, nampo pa kulapa ife kwene kwene mtipelekele ng'amba yabwino, umo sitilandilile vipacho va jiko pa nyengo yao; ndipo tijiyeluze pa kulangidwa kwanu

zene: Mtipulumuche ni mtivuule, pa manja ya wa mawongo watu, tikupembezani pa kujichicha; mchepekeche kujitwinya kwao, mtime usokolo wao, ndi mtimbilikanye malindi ayo wapanga; kuti ife tika-kala ndi kuombelela kwanu kwa nkondo yatu, tili-ndilidwe mmwemoje vipandu vonche, tikukuzeni, pakuti Imwe moka mpeleka kulaka konche; kwa ivo vakuyenela va Mwana wanu yeka yeka, Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Pa nyengo ya Mtimbo uli wonche kapena Kudwala konche kwakuyenela kwa wantu.*

Mlungu Mwene mpavu zonche, pa kukwiya mdapeleka mtimbo pa kamu lanu mwawenu mmapululu, chifuko wadamasula mwendo kwa Moses ni Aaron ni mbwinya yoka yoka; sonincho, nyengo ya mfumu David, mdawapa ni mtimbo wa chipindupindu maelfu ma kumi asano ni awili, nampo kukumbukila lisungu lanu mdawapulumucha yawo wanachala; Mtilengele lisungu ife wene zambi wosauka, yapo mnatipenyela ni kudwala kwakukulu ni kufa kwakunyinji: ndipo ngati siku zija mdalola voteteza, ndipo mdamuza Malaika yuja wakuonanga asiye kulanga, chimwechi chapano mkalole kubweza pa ife mtimbo uu ni kudwala kwakupwetekecha; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Pa Weeks za Ember, likadanenedwa siku lili lonche, kuwapempela yawo salovyedwe pa Holy Orders.*

Mlungu Mwene mpavu zonche, Atate watu wa kumwamba mnajigulila Church lakuyenela konche konche kwa mwazi wene mtengo wa Mwana wanu wokondedwa; Mlipenye Church limwelo ni lisungu, ndipo siku izi mlilangizile njila ni kuichogozza mitima ya wopotela wanu AAskof ni Wakuwesa gulu lanu la mbelele, kuti asamwikila ali yenche manja kuwilima, nampo wasankule ni mvano ni njeru wantu wakuyenela wapotele pa kulindilila kwa pa koka pa Church

lanu. Ndi mwaninke yawo saikidwe pa misinku yao kwa nchito ili yonche ya pa yoka neema yanu ni mwawi wanu wa Kumwamba; kuti pa machitidwe ni mayaluzo yao wabukiche kukuzika kwanu, ndipo wauchogoze upulumuchi wa wantu wonche; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kapena ili.*

Mlungu Mwene mpavu zonche, wakupembezani vonche vachomwe vabwino, kwa malango yanu pakukala Mlungu mwayalangiza maikidwe pa misinku ina ina pa Church lanu; mwaninka wonche yawo satanidwe kwa nchito yoyenela ili yonche kukutumikilani kuli konche mmwemo neema yanu, tikupembezani; ndipo mwazaziletu achiwo chimwechi ndi va zene zene va mayeluzo yanu ndi mwaveke ni umoyo wosalakwa, kuti wapotele pachogolo panu kwa kuvomeleka, Jina lanu lalikulu likuzidwe, ni kulikomela Church lanu la pa loka; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

¶ *Pempelo ilo liloleka kunenedwa pambuyo pa lili lonche la ayo pamwamba.*

Mlungu, chiyambile chitulo chanu ni ivo muli navo mwalengela lisungu ni kulekelela, myalandile mape-mbezo yatu yakujichicha; ndi ingakale tamangidwa ni kunyembedwa ndi mnyololo wa zambi zatu, maganigani ya lisungu lanu lalikulu nampo yatimasule; Yesu Kristo alemekezedwe, Wotiteteza watu ni Woimilila. *Amen.*

¶ *Pempelo kwa 'High Court of Parliament,' ilo likadawerengedwa yapo bwalo lao liungidwa.*

Mlungu mwene neema viwi viwi, tikupembezani kujichicha nditu kwa Ufumu uu ponche ponche, ndi maka maka kwa High Court of Parliament, ilo laungidwa siku izi panchi pa Mfumu watu mwene religion nditu ni mwene neema; Kutu mlole kuchogozza ni

kukazikicha mapangano yao yonche, mpunde kukuzidwa mawenu, Church lanu lipate ubwino, ni Sovereign watu, ni milaga yake, akale wosaluswa, ni mmbili yabwino, ni kufwanikila; kuti vonche viikidwe pa misinku yao ni kulimbichidwa wakachita likwale achiiwo, kuchamila vija vakupunda ni vakulimba, kuti mtendele ni kukondwa, va zene ni kuchita malinga, religion ni ubale wene wene, vilimbichidwe pa ife kwa vibadwa vonche. Ivi ni vonche vina ivo sivikadasiidwa, kwa achiiwo, kwa ife tawefe, ni kwa Church lanu la mpumpu, ife pakujichicha tipempa pa Jina ni Kuteteza kwake Yesu Kristo Ambuyatu woyelekedwelatu ni Mpulumuchi. *Amen.*

¶ *Collect kapena Pempelo kwa makalidwe yonche ya wantu ilo likadatimidwa pa nyengo zija yapo Litania losalangizidwa linaledwe.*

Mlungu, Wakupanga ni Wakusunga wana wa adam wonche, tikupembezani pa kujichicha kwa makamu yonche ni makalidwe ya wantu; kuti mlole kuwajiwicha njila zanu, ni kulama kwanu kwene kusangalalicha kwa mafuko yonche. Maka maka, tipempa kuti Church Katoliko likazikike; ndipo Roho wanu wabwino alilangizile njila ni kuliongola, mpaka wonche yawo wajivumbula ndi wajitana Wa Kristo wachogozedwe mnjila mwa zene ndi wagwili-letu mvano pa roho iyo ili imoji, kumangichana pa mtendele, ni kuchita malinga kwa kulama pano. Pomalizika, tipeleka mmanja mwanu, ngati pa manja ya Atate wabwino, wonche yawo wasauchidwa muli monche, kapena wafinyikizidwa, pa mtima, pa tupi, kapena pa makalidwe yao; [*\* maka maka yawo kwa chifuko chao yafunidwa mapempelo yatu,*] kuti chikukondweleni kwatontoza ndi kuwatengela mankwala umo viwasowela mwina mwina, kuwaninka kujizinga

\* *Aya yakadanenedwa yapo alipo wantu yawo wafuna mapempelo ya Gulu la Church.*

pa mapwetekecho yao, ni kutuluka kwa kusekelela pa masauko yao yonche. Ni ichi kwa chifuko cha Yesu Kristo tichipempa. *Amen.*

## MAU YA KUYAMIKA.

¶ *Yakuyamika kwa wonche ngati kamu.*

Mlungu Mwene mpavu zonche, Atate wa malisungu yonche, ife akapolo wanu wosayenela kantu tikuyamikani kujichicha ni kuchokela pa mtima kwa ubwino wanu wonche ndi ubale wanu wakukonda kwa ife, ni kwa wantu wonche; [*\*maka maka yawo wafunawo kutila nchembe ya kulumba ni kuyamika kwa malisungu yanu ayo mnawalengela siku izi.*] Tikuyelekelani pakuti mwatipanga, pakuti mwatisunga, ndi pakuti mwatininka vonche va mwawi va umoyo wa pano; nampo maka maka, pakuti mnakonda mosawelengeka apo mdaliombola jiko lino mkati mwa Ambuyatu Yesu Kristo; kwa ivo vakutitengela neema, ni kwa chikulupi cha kukuzika. Ndipo, tikupembezani, mtininke ife kuvela malisungu yanu umo tiyeneledwela, kuti mitima yatu iyamike yopanda kuzimbaicha, ndi tibukiche kulumba kwanu, si pa milomo yatu yoka, nampo pa makalidwe yatu; pa kujivumbukicha kukupotelani, ndi pa kuyenda-enda pachogolo panu pa kukala pa toka ni pa kuchita malinga siku zatu zonche; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu, uyu, pamoji ndi imwe ni Mzimu Woyela alemekezedwe ndi akuzidwe, mpaka vyaka vosata. *Amen.*

*Kwa vula.*

Mlungu Atate watu wa Kumwamba, pa kupe-nyelela vonche kwanu kwene neema mvumbicha vula

\* *Aya yakadanenedwa apo wena yawo wanapempelidwa wafuna kubwezela malumbo.*

ya chizimalupya ni vula ya kamkonda pa jiko, lituluche vipacho wavitumile wantu; Tikuyamikani pa kujichicha kuti mwakonda, apo vintu vitisowa nditu, kutipelekela pomalizika vula ya kukondecha pa jiko la chokolo chanu, ndipo kulipumicha apo lidauma, ife akapolo wanu wosayenela kantu titontozedwe, ni Jina lanu loyela likuzike: kwa malisungu yanu mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kwa ng'amba yabwino.*

Ambuye Mlungu, mwatichicha ife kwa malinga kwa mtimbo wanu wa masiku yano ya vula ya chibindikiza ni maji, ndipo pa lisungu lanu mwapumicha ni kutontoza maumoyo yatu kutitengela mpepo ina ya kukonda pa nyengo ii ni yene mwawi; Tililumba ni kulikuzicha Jina lanu la pa loka chifuko cha ili lisungu lanu, ndipo sitifotokoze siku zonche ubale wanu kwa chibadwa ni chibadwa; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kwa chindimba.*

Atate mwene lisungu lalinyinji, kwa ubwino wanu wene neema mwavela mapempelo yakulambalamba ya Church lanu, ndipo mwatembenuza chilala chatu ni kusowa vintu vikale kosauma malonda ni kuchuluka vintu; Ife tikuyamikani pa kujichicha kwa kukoma pa kosi kwanu kwa nyengo ii yoka; tikupembesani msasia ubale wanu wakukonda kwa ife, ndipo jiko latu litininke vipacho vake va kuonjezeka, mkuzike imwe ni ife titontozedwe: mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kwa Mtendele ni kuvutidwa kwa mawongo watu.*

Mlungu Mwene mpavu zonche, muli chilindo cha mpavu kwa akapolo wanu kwa nkope za wa mawongo wao; Tikulumbani ni kukuyamikani pakuti tavuulidwa pa vipandu vija vavikulu va pa danga, ivo vidatikweteza: Titulucha kuti kwa ubwino wanu

woka sitinavumbukichidwa ngati vofufula mmanja mwao; Tikupembesani msasia kutitengelancho ife malisungu aya yanu, ndipo jiko lonche lijiwe kuti imwe muli Mpulumuchi watu ndi Wotivuula kwa mpavu; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kwa kubwezela kwatu Mtendele kwa kamu.*

Mlungu wa chikalile mmwemoje, Atate watu wa Kumwamba, imwe moka mehita wantu kuilana bwino pa nyumba, ndi kutontoza punjo ya kamu la njalale losava lumbwe; Tiliyerekela Jina lanu loyela, kuti mwalola kuchicha mtima pa mapokoso ayo ya kumasula mwendo, ayo yauchidwa pa ife siku izo; tikupeembesani pa kujichicha viwi, kuninka ali yenche wa ife neema, kuti chiyambile chapano tivele bwino kuyenda chiyendele pa matauko yanu ya pa yoka; ndi takale ni umoyo wopanda milandu, ndi wa mtendele pa maso panu ni wene mbiri yabwino, tisapuma kukutililani nchembe yatu ya kulumba ni kuyamika kwa aya malisungu yanu kwa ife; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kwa Kupulumuchidwa kwa Chipindu-pindu, kapena Kudwala kwina kwakuyenela.*

Ambuye Mlungu, mwatitema mabala chifuko cha zambi zatu, ndipo mwatilaza chifuko cha volakwa watu, kwa kupenyela kwanu kwa kulemela masiku yano ni kwa kuofya; ndi chapano, pakati pa kulamula mwakumbukila lisungu, ndi kuyaombola maumoyo yatu pa kamwa pa nyifa; Tikutililani, Atate wabino, tawefe, maumoyo ni matupi aya mwayavuula, yakale nchembe yene umoyo kwanu, kulumba ni kukuzicha siku zonche malisungu yanu pakati pa Church lanu; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*

*Kapena ili.*

Ife tijichicha-panchi ndipo tivomela pa maso yanu, Atate mwene mwene lisungu, kuti malangidwe

yonche ayo yanalembedwa pa torah yanu yakadati-gwela umo tinayeneledwela chifulo cha volakwa watu va makamu makamu ni mtima wouma: Nampo pa kuona kuti ife tidajichicha panchi, ingakale wosajichicha ni likwale umo tinayeneledwela, mwakonda kwa lisungu lanu kutila mankwala pa kudwala kuja kwa kuyambukila uku tapwetekechedwa viwi nako masiku yano, ndi mwabweza mapokoso ya kusekelela ni kusangalala mmaseli mwatu; Tikutililani pa Ukulu wanu wa Mlungu nchembe ya kulumba ni kuyamika, kulumba ni kulikuzicha Jina lanu lakukuzika, kwa kulindilila kwanu mmwemo ni kupenyelela kwanu kutichinga ife; mkati mwa Yesu Kristo Ambuyatu. *Amen.*